# KUTSEKEREDWA NDI KUBWEZEREDWA KWA ANTHU OTHAWA KWAWO KU SOUTH AFRICA

Pitani patsamba lathu kuti mudziwe zambiri za nkhaniyi:
www.scalabrini.org.za

## KUTAMANGITSIDWA KWA OTAWA KWAWO KUMAYENDETSEDWA BWANJI MU SOUTH AFRICA?

Tikulangiza MWAMPHAMVU kuti, ngati mwatsekeredwa, mulandire thandizo lazamalamulo. Zimenezi ndizofunikira makamaka ngati mayimitsidwa kukhoti pasanathe maola 48 m'mbuyo mwa kumangidwa kwanu.

Ngati mwapempha chilolezo chachitetezo (ngati pali chiopsezo chozunzidwa kapena kuvulazidwa mukamabwerera kudziko lanu), simungathe kuthamangitsidwa. Pezani thandizo lazamalamulo mwachangu.

**SITEPE 1**

Wapolisi yekha kapena ofisala oyang'anira za anthu olowa m'dziko ndi kutuluka m'dziko ndi amene ayenera kukufunseni kuti munene kuti ndinu ndani. Ngati ali ndi 'zifukwa zomvetsetseka' zoganizira kuti ndinu okhala mudziko la South Africa mosatsatira malamulo, akhoza kukufunsani mafunso komanso kukumangani kwa nthawi yosapitilira maola 48 pa nthawi akuyang'ana ngati mukukhala mu South Africa potsatira malamulo. Pezani thandizo lazamalamulo!

**SITEPE 2**

Oyang'anira za anthu otuluka ndi kupita mu dziko ndi yekha ali ndi udindo wokuuzani kuti 'muli mlendo wasaloledwa'. Ndiyeno kuthamangitsidwa kwa anthu m'dziko kudzayamba. Mudzalembedwa chidziwitso cha zimenezi muchilankhulo chomwe mumamva bwino. Mudzaperekedwanso chidziwitso choti muli ndi ufulu wotsutsanandi chigamulo chimenecho. Woyang'anira za anthu otuluka ndi kupita mudziko akhoza kukumangani kuti azikubwerezani kudziko lanu - zili kwa iwo kuchita zimenezo.

**SITEPE 3**

Muyenera kubweretsedwa, inu nokha, kukhoti. Ayenera kuchita zimenezi pasanapitilire nthawi ya maola 48 kuyambira pamene mamangidwa kapena kutsekeredwa. Kenako khoti lidzagamulapo ngati muyenera kutsekeredwa m'ndende kapena ayi. Chigamulocho chiyenera kuperekedwa kwa inu mwa kulemba. Atha kuwonjezera nthawi yanu yotsekeredwa m'ndende mpaka masiku 30.

**SITEPE 4**

Pambuyo pa masiku 30 oyambirira, woyang'anira za anthu otuluka ndi kupita mudziko akhoza kupempha a kukhoti kuti aziwonjezerepo masiku 30 pa nthawi ndi nthawi muli mundende. Muyenera kukaonekera kukhoti, ndi kudziyimira kumeneko molemba. Nthawi yomwe mudzatsekeredwa mundende ikhoza kuwonjezeredwa ngati pali ndi zifukwa zomveka bwino zochita zimenezo. Mukhoza kumangidwa kwa masiku 120 onse.

**SITEPE 5**

Ngati asankha kukutamangitsani, mudzasamutsidwa ku Lindela Repatriation Centre ku Gauteng. Kunena zoona, zimenezi zikhoza kutenga nthawi yaikulu, ndipo mukhoza kutsekeredwa kwa a polisi kapena kundende muyimira kusamutsidwa kumeneko kapena kudzikoli limene munachokera. Popeza muli ndi ufulu wanu mundende (onani tsamba lotsatira), kukhala ku Lindela ndi malo ena otsekeredwa anthu si kwabwino.

**SITEPE 6**

Panthawiyi, Dipatimenti ya Home Affairs ikambirana ndi ofesi ya kazembe wanu kapena oyang'anira olowa m'dziko lanu kuti akonzekere kubwerera kwanu. Amafuna kuonetsetsa kuti mwalandiridwa pobwerera.

**STEP SEVEN**

Musanabwezedwe kudziko lanu, mudzapereke dwa chidziwitso choti mudzabwezedwa kudziko lanu. Ayenera kugwiritsa ntchito basi, sitima kapena ndege pokubwezerani kudziko la nu. Mukathamangitsidwa, ndizotheka kuti mudzaletsedwa kubwerera kudziko la South Africa mpaka zaka zisanu. Ngakhale pambuyo pa nthawi imeneyi, kuletsedwa kumeneko kuyenera kuwononga mwayi wanu wopatsidwa visa mu South Africa.

Pa nthawi yokonzekera kubwezedwa kwanu, muyenera kukonza zochoka ku South Africa nokha, ngati mungatsimikizire kuti muli ndi ndalama komanso zikalata zoyendera. Ngati mwaloledwa, mudzapatsidwa fomu yoti mupereke nayo lipoti ku dipatimenti ya Home Affairs pa nthawi ndi nthawi. Ngati mungathe kukonzekera kuchoka nokha ku South Africa, tikukulimbikitsani kuti mutero - ngati kuchita zimenezo sikudzakupatsani ziopsezo.

Kumbukirani kuti ngati mwakhala mundende kwa masiku 120 musanabwezedwe kudziko lanu, muli ndi ufulu womasulidwa.

## 1. NDI LITI PAMENE MUNTHU ANGAMANGIDWE CHIFUKWA CHOSOWA ZIKALATA ZOYENERA?

Ku South Africa, apolisi ndi oyang'anira za kutuluka ndi kulowa kwa anthu mudziko ndi OKHA omwe amaloledwa kukufunsani kuti muwonetse zitupa. Zikalata zimenezo zimaphatikizapo zosonyeza dzina lanu ndi zitupa. Mutha kumangidwa kokha ngati wapolisi kapena woyang'anira zakutuluka ndi kulowa kwa anthu mudziko akukhulupirira 'pazifukwa zomveka' kuti mukukhala ku South Africa mosaloledwa.

## 2. MONGA WOSAKHALA NZIKA YAKU SOUTH AFRICA, NDI ZOLEMBA ZITI ZOMWE NDIYENERA KUKHALA NAZO NTHAWI ZONSE?

Ngati muli ndi visa mu pasipoti yanu, nthawi zonse muyenera kunyamula makamaka kopi yovomerezeka ya pasipoti ndi visa. Ngati ndinu othawa kwawo ovomerezeka, mutha kukhala ndi chikalata chosonyeza zimenezo nthawi zonse. Ngati muli ndi Asylum Seeker Temporary Permit, mutha kukhala ndi chikalata chenicheni nthawi zonse.

## 3. KODI NDIKHOZA KUTSEKEREDWA KUTI NDISANABWEZEDWE KUDZIKO LANGA?

Mutha kutsekeredwa pamalo osankhidwa ndi Director General wa Home Affairs (Izi zinasindikizidwa mu Gazette ya Boma). Malowa akuphatikizapo malo apolisi, malo osungira anthu ndi maofesi omwe amayang'aniridwa ndi oyimira kapena enieni a dipatimenti ya Home Affairs. Nthawi zambiri okonzeka kubwezeredwa amasamutsidwa ku Lindela Repatriation Centre ili m'chigawo cha Gauteng, malo okhawo yosungira anthu osaloledwa ku South Africa.

## 4. KODI UFULU WANGA NDI WOTANI PAMENE NDILI M'NDENDE?

Ufulu wanu m'ndende umaphatikizapo: (1) Kudziwitsidwa zifukwa zomwe mwatsekeredwa komanso ufulu wanu m'ndende; (2) Kutsekeredwa m'mikhalidwe yoyenera anthu yomwe imaphatikizapo malo ogona, chakudya, zowerengera, chithandizo chamankhwala; (3) Kukhala ndi ufulu wosankha loya omwe mukufuna, kapena kuthandizidwa ndi loya wa Boma; (4) Kuchezeredwa ndi mwamuna kapena mukazi wanu, wachibale wanu, alangizi osankhidwa achipembedzo kapena madokotala; komanso (5) Kusasungidwa m'malo amodzi ndi oganiziridwa za zigawenga.

## 5. KODI NDINGAPEZE BWANJI CHITHANDIZO CHALAMULO NDILI M'NDENDE?

Ngati mwamangidwa kapena kutsekeredwa mundende, tikukulangizani mwamphamvu kuti mupeze thandizo lazamalamulo. Muli ndi ufulu wakuchezeredwa ndi mwamuna kapena mukazi wanu, wachibale wanu, ndi kusankha alangizi achipembedzo omwe angakuthandizeni kupeza thandizo lazamalamulo. Ngati simungathe kulipira loya, muyenera kulumikizananso ndi bungwe lopanda phindu, lomwe linalembedwa pansipa. (Dziwani kuti, ngati mwamangidwa chifukwa cha mlandu, mutha kupempha Chithandizo Chazalamulo.)

## 6. NDANI SANGABWEZEREDWE KUDZIKO LAKE?

Ofunafuna chitetezo ndi othawa kwawo sangabwezeredwe kumayiko awo pansi pa Lamulo La Otuluka ndi Olowa M'dziko, chifukwa kuchita zimenezo kungakhale kuphwanya ufulu wa anthu (lomwe lili lamulo loti Mayiko saloledwa kubwezera anthu omwe ali pachiopsezo chovulazidwa kapena kufa ku maiko awo). Izi zikuphatikizapo anthu omwe akufuna kupempha chitetezo. Komabe ofunafuna chitetezo omwe pempho lawo likanidwa ndipo sanatsutse chigamulo chakukanidwa kwa pempho lawo akhoza kutsekeredwa komanso kubwezeredwa kumayiko awo. Kutsekeredwa kwa ana ang'ono sikololedwa - koma zimenezo zikhoza kuchitika ngati 'palibe njira ina iliyonse'. Izi zimachitika potsatira zotetezera zina.

## 7. KODI KUBWEZEREDWA KWA ANTHU KUMAYIKO AWO KUMAYENDETSEDWA BWANJI KWENIKWENI?

Chaka chilichonse dipatimenti ya Home Affairs imabwezera anthu masauzande kumayiko awo. Ngakhale pali chitetezo chalamulo, akaidi ambiri ku Lindela amakumana ndi zovuta kwambiri. Zapezeka kuti omangidwa amasungidwa kwa masiku opitilira 120 pansi pamikhalidwe yovuta kwambiri, kuphatikiza vuto lakuchepa kwa mwayi wopeza chithandizo chamankhwala, upangiri wamalamulo komanso kutsekeredwa kosalolodwa kwa ofunafuna chitetezo ndi ana ang'ono.

## 8. NDIKUFUNA THANDIZO. NDINGALANKHULE NDI NDANI?

Lawyers for Human Rights | Durban: 031 301 0531
| Pretoria: 012 320 2943
Johannesburg: 011 3391960
Refugee Rights UCT | 021 650 5581
The Scalabrini Centre of Cape Town | 021 465 6433

Scalabrini Centre of Cape Town
WWW.SCALABRINI.ORG.ZA

SONKE GENDER JUSTICE
HIV/AIDS • GENDER EQUALITY • HUMAN RIGHTS
WWW.GENDERJUSTICE.ORG.ZA